## PHUNZIRO LA 41

1. Kodi chifukwa chiyani Mulungu amalankhulana ndi anthu?
-Kuti anthuwo apulumutsidwe.

2. Kodi chifukwa chiyani Mulungu ankafuna kuti Yona apite ku mzinda wa Nineva?
-Chifukwa chakuti Mulungu ankaŵakonda anthu a ku Nineva.
-Chifukwa chakuti Mulungu ankafuna kuti aŵapulumutse anthu aku Nineva ku mphamvu ya sambi, imfa ndi Satana.

3. Kodi chifukwa chiyani Yona anathaŵa?
-Yona anathaŵa chifukwa chakuti iye sankafuna kuti apite ku mzinda wa Nineva.

4. Kodi chifukwa chiyani Yona sankafuna kupita ku mzinda wa Nineva?
-Chifukwa chakuti anthu a ku Nineva anali oyipa kwambiri.
-Chifukwa chakuti anthu a ku Nineva anali adani a a Isirayeli.
-Chifukwa chakuti Yona sankafuna kuti Mulungu aŵapulumutse anthu a ku Nineva.

5. Kodi Yona anatha kumuthaŵa Mulungu?
-Iyayi.

6. Kodi Yona anatha kubisala pa maso pa Mulungu?
-Iyayi.

7. Kodi Mulungu anachita chiyani pa nthaŵi imene Yona sanamumvere Iye posapita ku Nineva?
-Mulungu anatumiza msomba yayikulu kukamumeza Yona.

8. Kodi Yona anakhala m'mimba mwa somba kwa masiku angati?
-Masiku atatu, usiku ndi usana.

9. Kodi Yona anatha kudzipulumutsa yekha m'mimba mwa somba yayikulu ija?
-Iyayi.

10. Kodi ndani amene anakatha kumupulumutsa Yona?
-Mulungu.

11. Kodi anthu onse akufanana bwanji ngati Yona?
-Anthu onse sangathe kudzipulumutsa okha ku mphamvu ya tchimo, imfa ndi Satana ngati m'mene sanathere Yona kudzipulumutsa yekha m'mimba mwa somba ija.
-Mulungu yekha ndi amene angathe kuŵapulumutsa anthu onse ngati m'mene anathera kumupulumutsa Yona.

12. Kodi Mulungu anachita chiyani pamene Yona anavomereza kuti sanamumvere ndipo  wamuchimwira Iye?
-Mulungu anayipangitsa msomba yayikuru ija kuti imulavulire pa mtunda.

13. Kodi Mulungu anamuwuza Yona kuti asapite ku Nineva atatha kumupulumutsa?
-Iyayi.



-Kodi Mulungu anakuvomereza kupembedza kwa mafano amene a Isirayeli ankaŵapanga aja?
-Iyayi.

-Kodi chifukwa chiyani?
-Chifukwa chakuti Mulungu anadziŵa kuti iwowo ankamupembedza Iye ndi pakamwa pawo pokha.
-Chifukwa chakuti Mulungu ankadziŵa kuti m'mitima mwawo ankaŵapembedza mafano.

-Kodi ndani amene amadziŵa zonse za m'mitima mwathu?
-Mulungu.

-Mulungu amatha kuwona m'mitima mwathu.

-Mulungu amadziŵa ngati tikupembedza Iye ndi pakamwa pathu pokha kapena ndi mitima yathu.

-Kodi Mulungu amalankhula chiyani za mitima yathu?
-Mulungu amalankhula kuti mitima yathu yonse yadzadza ndi machimo.

-Ngakhale kuti a Isirayeli ambiri ankapembedza zosema, kodi panali a Isirayeli ena amene ankampembedza Mulungu?
-Inde.
-Analipo pang'ono.

-A Isirayeli amene ankampembedza Mulungu, ankayembekezera kuti Mulungu adzatumiza Mpulumutsi.

-Aneneri a bodza ankanena kuti iwowo ankanena zowona za Mulungu, koma ankanena za bodza za Satana.

-Aneneri a bodza ankanena kuti Mulungu sapereka chilango pa machimo awo.

-Kodi ndani amene ankalankhula kudzera mwa aneneri a bodza?
-Satana.

-Lero, Satana ndi yemweyo.

-Lero, Satana akupitirizabe kulankhula bodza lache kudzera mwa anthu.

-Satana akulankhula kudzera mwa anthu kuti asamamutsate Mulungu.

-Satana akulankhula kudzera mwa anthu kuti adzitsata njira za makolo.

-Satana akulankhula kudzera mwa anthu kuti asamamvere mawu a Mulungu.

-Satana akulankhula kudzera mwa anthu kuti mawu a Mulungu ndi abodza.

-Satana akulankhula kudzera mwa anthu kuti Mulungu sadzapereka chilango pa tchimo.

-Ngakhale kuti a Isilayeli ankapembedza zosema zimene anazipanga, nawo Aneneri a Mulungu ankapitiliza kumpembedza Mulungu M’nyumba Yache.



-Mulungu sanasinthe.
-Mulungu sasintha.
-Mulungu ankafunabe kuti Yona apite ku Ninefa.

14. Kodi anthu a ku Nineva anaŵamvera mawu a Mulungu amene Yona anaŵawuza iwowo?
-Inde.

15. Kodi amuna amene anasankhidwa ndi Mulungu kuti akhale atumiki ache ndikumaŵawuza anthu mawu ache ankatchedwa kuti ndani?
- Aneneri.

16. Kodi aneneri ameneŵa, ankaŵawuza chiyani anthu?
-Ankaŵawuza kuti Mulungu akufuna kuti iwowo asiye njira zawo za machimo ndipo adzitsata njira ya Mulungu.

17. Kodi chidzachitike ndi chiyani kwa mitundu khumi ya ku Isirayeli ija ngati iwowo sakutsata njira ya Mulungu?
-Mulungu adzaŵatumiza a Siliya kudzaŵagonjetsa iwowo pa nkhondo, ndikuŵachita ngati akapolo awo.

18. Kodi chidzachitike ndi chiyani kwa mitundu iŵiri ya ku Yuda ija ngati iwowo sakutsata njira ya Mulungu?
-Mulungu adzaŵatumiza anthu a ku Babeloni kudzaŵagonjetsa iwowo pa nkhondo, ndikuŵachita ngati akapolo awo.

-Ngakhale kuti zaka zambiri zinapita, Mulungu chiperekereni lonjezo lotumiza Mpulumutsi, kodi Mulungu analiyiŵala onjezo lache?

-Iyayi.

-Mulungu anamulonjeza Adamu ndi Hava kuti adza-tumiza Mpulumutsi.
-Mulungu anamulonjeza Aburahamu, Isaki ndi Yakobo kuti adzatumiza Mpulumutsi.
-Mulungu anamulonjeza Mose ndi a Isirayeli kuti adza-tumiza Mpulumutsi.
-Mulungu anamulonjeza Mfumu Davide ndi Solomoni kuti adzatumiza Mpulumutsi.

-Mulungu sanaliyiŵale lonjezo lache lotumiza Mpulumutsi.

-Ngakhale kuti a Isirayeli sankamukhulupilira Mulungu, kodi Mulungu anaganiza zosatumiza Mpulumutsi?
-Iyayi.

-Ngakhale kuti a Isirayeli sankamukhulupilira Mulungu, kodi chifukwa chiyani Mulungu anaganizabe zotumiza Mpulumutsi?
-Chifukwa chakuti Mulungu amaŵakonda anthu onse.
-Chifukwa chakuti Mulungu akufuna kuti aŵapulumutse anthu onse ku mphamvu ya tchimo, imfa ndi Satana.
-Chifukwa chakuti Mulungu sakufuna kuti munthu wina aliyense apite ku Nyanja ya Moto Wosatha.

-Kodi Mulungu anapereka kwa ndani uthenga wa Mpulumutsi amene ankabwerayo?
-Kwa Aneneri.

-Kodi ma uthenga amene Mulungu anaŵapereka kwa Aneneri onena za Mpulumutsi amene ankabwerayo ankalembedwa kuti?



-Mulungu asanamutumize Mpulumutsi, anakhoza kale zonse zimene zidzamuchitikire Mpulumutsiyo.

-Aneneri a Mulungu anaŵawuza a Isirayeli za Mpulumutsi amene Mulungu amkamutumizayo.

-Aneneri a Mulungu ankaŵawuza a Isirayeli kuti asiye njira ya machimo ndikumatsata njira ya Mulungu.

-Koma a Isirayeli ambiri anakana kuŵamvera Aneneri a Mulunguwo.

-M’malo mwache a Isirayeli ankaŵapha Aneneri a Mulunguwo.

-Kodi chifukwa chiyani a Isirayeli ankaŵapha Aneneri a Mulunguwo?
-Chifukwa chakuti Aneneri a Mulungu ankaŵawuza a Isirayeli kuti asiye njira za machimo ndikumatsata njira ya Mulungu.
-Chifukwa chakuti Aneneri a Mulungu ankaŵawuza a Isirayeli kuti Mulungu adzaŵalanga ndi imfa chifukwa cha machimo awowo.

-Chifukwa chakuti a Isirayeli amkaŵakonda machimo awowo, iwo sankafuna kumumvera Mulungu.

-M’malo moŵamvera Aneneri a Mulungu, a Isirayeli ankaŵamvera Aneneri a bodza.

-Aneneri a bodza ankalankhula kuti iwowo anali Ane-neri a Mulungu, koma ali a Satana.

-Kodi china ndi chiyani chimene analankhula Mulungu chonena Mpulumutsi amene ankamutumizayo?

Tiyeni tiŵerenge Yesaya 53:9

9-Ndipo anaŵayika manda ache pamodzi ndi anthu osalungama, ndiponso ndi olemera mu imfa Yache , ngakhale kuti Iye sanachite chisokonezo, ndiponso mkamwa mwache munalibe bodza.

-Mulungu analankhula kuti Mpulumutsi adzayikidwa m'manda pamodzi ndi anthu olemera.

-Kodi china ndi chiyani chimene analankhula Mulungu chonena Mpulumutsi amene ankamutumizayo?

Tiyeni tiŵerenge Masalimo 16:10

10-Chifukwa chakuti sadzandisiya Ine ku manda, inu simudzamusiya oyera wanu kuti awole.

-Mulungu analankhula kuti Mpulumutsi adzadzuka kuchokera kwa akufa.

-Kodi china ndi chiyani chimene analankhula Mulungu chonena Mpulumutsi amene ankamutumizayo?

Tiyeni tiŵerenge Masalimo 68:18

18-Pamene munakwera kumwamba, munaŵatsogolera akayidi mnjira yanu.

-Mulungu analankhula kuti Mpulumutsi adzabwelera kumwamba.



-M'buku la Mulungu7, Bayibulo.

-Mulungu asanatumize Mpulumutsi, Mulungu anali atakonza kale zonse zimene zidzamuchitikire Mpulumutsiyo.

-Kodi Mulungu anati chiyani za Mpulumutsi amene ankabwerayo?

Tiyeni tiŵerenge Yesaya 9:7a

7a-Zowonjezera za ulamuliro ndi mtendere wache sizidzakhala ndi malire. Iye adzalamulira pa udindo wa Davide ndi kuwukhazikitsa ufumu wache ndiponso kuwuteteza ndi chilungamo ndi kulungamika kuchokera mu nthaŵi imeneyo mpaka kalekale.

-Mulungu analankhula kuti Mpulumutsi adzakhala chidzukulu cha Davide ndiponso adzakhala Mfumu mpaka kalekale.

-Kodi china ndi chiyani chimene analankhula Mulungu chonena Mpulumutsi amene ankamutumizayo?

Tiyeni tiŵerenge Yesaya 7:14

14-Namwali adzakhala ndi pathupi ndipo adzabereka mwana wamamuna, amene adzamutcha dzina lache Emanuwelo.

-Mulungu analankhula kuti Mpulumutsi sadzakhala ndi bambo ake a ku thupi, kapena mayi a ku thupi, koma adzabadwa mwa namwali.

-Kodi china ndi chiyani chimene analankhula Mulungu chonena Mpulumutsi amene ankamutumizayo?

Tiyeni tiŵerenge Mika 5:2

2-“Koma iwe Betelehemu Efurata, ngakhale uli wamng’ono pakati pa mitundu ya ku Yuda, kuchokera mwa iwe, adzaturuka wina olamulira Isirayeli, chiyambi chake chili chochokera mu nthaŵi ya kale.”

-Mulungu analankhula kuti Mpulumutsi adzabadwira mu mzinda wa Betelehemu.

-Kodi china ndi chiyani chimene analankhula Mulungu chonena Mpulumutsi amene ankamutumizayo?

Tiyeni tiŵerenge Hoseya11:1

1.”Pamene Isirayeli anali mwana, Ine ndinamukonda, ndipo ku Iguputo ndinamuyitana mwana wanga wamamuna.”

-Mulungu analankhula kuti adzamuyitana Mpulumutsi kuchokera ku Iguputo.

-Kodi china ndi chiyani chimene analankhula Mulungu chonena Mpulumutsi amene ankamutumizayo?

Tiyeni tiŵerenge Yesaya 11:2

2-Mzimu wa Ambuye udzakhala pa Iye, Mzimu wa mzeru ndi kumvetsetsa, Mzimu oyanjanitsa ndipon-



18-Anagaŵana zovala Zanga pakati pawo ndipo analondora mawula pa zovala zanga.

-Mulungu analankhula kuti anthu adzawombeza mawula pa zovala zache.

-Kodi china ndi chiyani chimene analankhula Mulungu chonena Mpulumutsi amene ankamutumizayo?

Tiyeni tiŵerenge Masalimo 22:6-7

6-Koma Ine ndi nyongolotsi, osakhala munthu, yoyinena anthu ndikunyozedwa ndi anthu.
7-Anthu onse ondiwona Ine akuseka, akundinyoza Ine, akugwedeza mitu yawo.

-Mulungu analankhula kuti Mpulumutsi adzasekedwa ndikunyozedwa.

-Kodi china ndi chiyani chimene analankhula Mulungu chonena Mpulumutsi amene ankamutumizayo?

Tiyeni tiŵerenge Yesaya 53:12

12-Chomcho, ndidzamupatsa Iye mbali pakati pa akulu akulu, ndipo adzagaŵana ndi a mphamvu zoyipazo, chifukwa chakuti anapereka moyo wache ku imfa, ndipo anamuŵerengera pamodzi ndi anthu ochimwa. Pakuti ananyamula machimo athu ambiri, ndiponso anaŵapemphelera ochimwa.

-Mulungu analankhula kuti Mpulumutsi adzakhala pamodzi ndi anthu osalungama.

-Mulungu analankhula kuti Ayuda adzamukana Mpulumutsi.

-Kodi china ndi chiyani chimene analankhula Mulungu chonena Mpulumutsi amene ankamutumizayo?

Tiyeni tiŵerenge Masalimo 69:4

4-Iwo ondida Ine palibe chifukwa, achuruka ngati tsitsi la m'mutu mwanga, ambiri ndi adani anga palibe chifukwa, amene akufuna kundiwononga Ine.

-Mulungu analankhula kuti Mpulumutsi adzadedwa popanda chifukwa.

-Kodi china ndi chiyani chimene analankhula Mulungu chonena Mpulumutsi amene ankamutumizayo?

Tiyeni tiŵerenge Masalimo 22:16

16-Agalu andizungulira ine, khamu la anthu osalungamika landizungulira Ine, andibowola manja ndi mapazi anga.

-Mulungu analankhula kuti manja ndi mapazi a Mpulumutsi adzabowoledwa.

-Kodi china ndi chiyani chimene analankhula Mulungu chonena Mpulumutsi amene ankamutumizayo?

Tiyeni tiŵerenge Masalimo 22:18



so wa mphamvu, Mzimu wodziŵa ndiponso owopa Ambuye.

-Mulungu analankhula kuti Mpulumutsi adzatsogoleledwa ndi Mulungu Mzimu Woyera.

-Kodi china ndi chiyani chimene analankhula Mulungu chonena Mpulumutsi amene ankamutumizayo?

Tiyeni tiŵerenge Yesaya 53:4-5

4-Koma Iye anasenza zosawutsa zathu, ndikusenzanso zowawa zathu, koma ife tinazitenga zowawazo ngati chilango chochokera kwa Mulungu., anamenyedwa ndi Mulungu, ndiponso anazumzidwa ndi Mulungu.
5-Koma Iye analasidwa chifukwa cha machimo athu, Iye anavulazidwa chifukwa cha kusakhulupilika kwathu, chilango chotibweretsera ife mtendere chili pa Iye, chifukwa cha mabala ache, ife tachilitsidwa.

-Mulungu analankhula kuti Mpulumutsi adzavutikira anthu onse.

-Kodi china ndi chiyani chimene analankhula Mulungu chonena Mpulumutsi amene ankamutumizayo?

Tiyeni tiŵerenge Masalimo 41:9

9-Ngakhale azinzanga eni eni amene ndimaŵakhulupilira, amene anaja mkate wanga, andiwukira.

-Mulungu analankhula kuti Mpulumutsi adzaperekedwa ndi mzache.

-Kodi china ndi chiyani chimene analankhula Mulungu chonena Mpulumutsi amene ankamutumizayo?

Tiyeni tiŵerenge Zakariya 11:12-13

12-Ine ndinaŵawuza iwo kuti, “Ngati inu mukuganiza kuti ndizabwino, mundipatse palipiro anga, koma ngati simukundipatsa, musunge.” Chomcho , Ine anandilipira ndalama makumi atatu.

13-Ndipo Ambuye analankhula ndi Ine kuti, “Ukaziponye ndalamazo kwa anthu owumba mbiya” – mtengo wache wabwino umene anandigulira Ine! Chomcho ndinatenga ndalama makumi atatu aja ndikuziponya kwa owumba mbiya Mnyumba ya Ambuye.

-Mulungu analankhula kuti Mpulumutsi adzagulitsidwa pa mtengo okwana ndalama makumi atatu.

-Kodi china ndi chiyani chimene analankhula Mulungu chonena Mpulumutsi amene ankamutumizayo?

Tiyeni tiŵerenge Masalimo 27:2

2-Anthu oyipa pofika kwa Ine kudzandigwira kuti andiphe, adzapunthwa ndi kugwa.

-Mulungu analankhula kuti Mpulumutsi adzamunamizira.

-Kodi china ndi chiyani chimene analankhula Mulungu



chonena Mpulumutsi amene ankamutumizayo?

Tiyeni tiŵerenge Yesaya 50:6

6-Ndinapereka msana wanga kwa anthu amene anandimenya, matsaya anga  kwa iwo amene ankazula ndevu zanga. Sindinabise nkhope yanga ku kunyozedwa ndi kulavulilidwa.

-Mulungu analankhula kuti Mpulumutsi adzalavulilidwa ndiponso kumenyedwa.

-Kodi china ndi chiyani chimene analankhula Mulungu chonena Mpulumutsi amene ankamutumizayo?

Tiyeni tiŵerenge Yesaya 53:7

7-Iye anavutitsidwa ndi kunyozedwa, koma Iye sanatsegule pakamwa pache; ngati mnkhosa yopita kukaphedwa, ndiponso ngati nkhosa pa maso pa woyipha, chomcho sanatsegule pakamwa Pache.

-Mulungu analankhula kuti Mpulumutsi sadzalankhula china chilichose pamene adzidzanyozedwa.

-Kodi china ndi chiyani chimene analankhula Mulungu chonena Mpulumutsi amene ankamutumizayo?

Tiyeni tiŵerenge Yesaya 53:3

3-Iye ananyozedwa ndikukanidwa ndi anthu, munthu wachisoni komanso odziŵa mavuto. Ananyozedwa ngati munthu omubisila anthu nkhope zawo, ndipo ife sitinamulemekeze.